

NYA_TTB_1107_SCRIPT

1 Yohane : 4:7-11

Mutu : Akristu ayenera kukondana wina ndi mnzake.

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolera ndi mau apa Yohane 3:20-21, amene akuti, “Pakuti yense wakuchita zoipa adana nako kuunika, ndipo sakudza kwa kuunika, kuti zingatsutsidwe ntchito zake. Koma wochita choonadi adza kuunika, kuti ntchito zake zionekere kuti zinacidwa mwa Mulungu.”

Mupologalamu yatha, tinali kukambirana pa 1 Yohane 4:5-9, pamene timapitiliza kuona kuti akristu ayenera kuchenjera ndi aphunzitsi onyenga. Ndipo lero pa 1 Yohane 4:7-11, tikambirana kuti akristu ayenera kukondana wina ndi mnzake.

7. Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa kuti chikondi chichokerakwa Mulungu, ndipo yense amene akonda, abadwa kuchokera kwa Mulungu, namzindikira Mulungu.

Tiyeni pano tigwire mau akuti, “Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake.” Ndiye mwina mwafunsa kale kuti kodi pali chifukwa

chanji kuti ife tikondane? Yankho likuti, inu ndi ine tiyenera kukondana chifukwa Mulungu ndiye chikondi. Pa yankho ili, ndifuna kuti inu ndi ine, tisamalitse kwambiri pachimene Yohane akunena. Taonani iye wangotsiriza kumene kuchenjeza za aphunzitsi onyenga, amene sayenera kukondedwa ngakhale kupemphereredwa chifukwa anasankha kukhala ana a m'dierekezi. Ndiye sibwinokumawatsitsa mtima kuti ndimakupemphererani ayi. Ife, tiyenera kupempherera ana a Mulungu ndi iwo amene asanamdziwe Kristu kuti alandire mau a Mulungu. Ndiye pamene Yohane wachoka kuchenjezo la aphunzitsi onyenga, tsopano watembenukira kuchiphunzitsi cha gawo lino, chomwe chikuti wokhulupirira ayenera kukondana wina ndi mnzake.

Pano ndiyenerakukumbutsa kuti Yohane sakukamba za chikondi chomwe chimakhala pakati pa mwamuna ndi mkazi kapena pakati pa makolo ndi ana ayi, koma chikondi chapaderadera, chochokera Kumwamba. Ichi, ndichikondi chomwe Mzimu Woyera amalonga mkati mwathu ndipo ndiMzimuwa Mulungu wokha womwe ungaonetsere chikondi chimenechi kwa ife. Kutsimikiza kuti

ndichikondi cha Mulungu ndipo kuti ndi Mzimu wa Mulungu wokha womwe ungapange ife kupereka chikondichi kwa anzathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna timvetsetse kuti ichi, sichikondi chomwe timangosangalatsidwa ndi anzathu ena kumakhalanawo ayi. Mwanjira ina tikunena kuti anthu ambiri takhala tikugwiritsa ntchito chikondi ichi, molakwika. Tikunena kuti anthu ambiri agwiritsa ntchito chikondi chokhala bwino ndi ena pakutembenuza kukhala chikondi pakati pa mwamuna ndi mkazi. Kunena kuti anthu ena akhala akumakhumudwa pamene agwiritsantchito chikondi ichi pakufunsira mkazi kuti alowe naye paukwati. Mwachisoni kuti mkazi amanena kuti iye amangocheza nawo chabe, koma sawakonda kuti akhoza kukhala nawo paukwati ayi.

Nkhani ikuti pamene inu mukumana ndi munthu Wobadwa kwatsopano, amakukondanimwamtundu wina mwanjira yoonetsa kuti ndiye Wobadwa mwa Mulungu. Kutanthauza kuti amakukondani ndi chikondi chochokera Kumwamba popeza Mulungu ndiye chikondi, kasupewachikondi, muzu wachikondi, kholo ndi mtsogoleri wachikondi. Kutsimikiza kuti chikondi ndipo

pokolowekapo chilamulo chonse ndipo kuti cholinga chonse cha chilamulo ndikukhala ndi chikondi pa Mulungu ndi munthu mnzathu. Ichi, ndichimene Yohane anati, “Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa kuti chikondi chichokerakwa Mulungu.” Tikunena kuti chikondi ndi lamulo lochokerakwa Mulungu ndipo kuti ndilo lamulo lomwe limaonetsa chifuniro chake chomwe ndichomkondweretsa mwini. Chikondi ichi, chimachokera kwa Mulungu mwini chimene chiri mphatso ya chisomo chake ndi chipatso cha Mzimu wake chomwe chimaphunzitsaokhawo wotembenuka mtima.

Apa, anali kunena kuti Mzimu wa Mulungu ndi Mzimu wa chikondi ndipo kuti moyo watsopano mwa ana a Mulungu ndicho chipatso cha chikondi. Paulo pa Agalatiya 5:22, anatsindika kunena kuti, “koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi...” Tikunena kuti munthu amene adziwa Mulungu kudzera mwa Kristu, amakonda iwo amene ali ndi chisomo cha Mulungu mkati mwawo ndi chithunzi cha Kristu pa iwo. Iyeyu ndiye adziwa mtima ndi chifuniro cha Mulungu chomwe chimaphunzitsidwa za kukonda abale. Kodi chipatso ichi, chimaoneka mwa inu?

8. Iye wosakondasazindikira Mulungu; chifukwa Mulungu ndiye chikondi.

Mtumwi Yohane akunenetsa kuti munthu amene sakonda ana a Mulungu, iwo amene anabadwa mwa Iye, sadziwa kukonda Mulungu yemwe ali Atate wawo. Kutanthauza kuti munthu uyu, alibe malingaliro abwino a Mulungu, ndipo ngati alibe ulamuliro wachikondi mwa iye, sayenera kudziika kukhala wofanana ndi Kristu. Popeza Kristu ndiye chikondi, osati kuti analandira chikondicho ayi, koma Iye ndiye chikondicho. Kutsindika kunena kuti Mulungu sasintha ngakhale dziko lisinthe, kaya tikhale m'dziko la chisokonekero, chisawawa ndi la m'dima.

Tsono nkhani yonseyi ikulingapaganizo la Yohane lakuti mphunzitsi wonyenga ndiye munthu amene alibe chikondi ndipo kuti Mulungu ndiye chikondi. Ndiye popeza munthuyu alibe chikondi, zikutanthauza kuti samdziwa Mulungu, kutsindika kuti munthuyu sadziwa chikondi. Koma njira imodzi yomwe inu mungaonetse kuti mumadziwa chikondi ndi yakuti inu mumakhudzidwa ndi moyo wa wokhulupirira mnzanu

9. Umochidaoneka chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anamtuma Mwana wake Wobadwa yekha, alowe m'dziko lapansi kuti tikhale ndi moyo mwa Iye.

Tsono Mtumwi Yohane mundime iyi, sakunena kuti palibe njira ina momwe chikondi cha Mulungu chimaonekera ayi. Iye akuti, mwanjira zochuluka momwe chikondi cha Mulungu chingaonetsedwe, koma imfa ya Mwana wake, momwe anachita kutumizidwa kuchokera m'Mwamba, ndiyo ikuonetsa poyera za chikondi cha Mulungu. Tamvani zomwe akunena pa Yohane 3:16, pamene akuti, “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asataike, koma akhale nawo moyo wosatha.”

Tsono Yohane akunena kuti chikondi cha Mulungu chinaonetsedwa pamene Ambuye Yesu anafa ndi cholinga chakuti ife wokhulupirira tikhale ndi moyo wamuyaya. Tikunena kuti ndichizindikiro chachikulu pa ife chakuti Mulungu atikondapakutumiza Mwana wake Wobadwa yekha ndi cholinga chakuti ife mwa Iye, tikhale ndi moyo. Ichi, ndichifukwa chakuti Kristu ndiye moyo popeza anaombola moyo wathu umene unataidwa kudzera

m'machimoathu. Tere chikondi chimenechi, ndichimene chiyenera kutikakamizaife kukonda wokhulupirira anzathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsakuti chikondi cha Mulungu ndi chodabwitsa popeza ifesitidamukonde, koma Iye ndiye adayambakutikonda. Kutanthauza kuti Mulungu anatikondaife ngakhale pamene ife tinalibe chikondi pa Iye, pamene ife tinali muuchimo, m'chisoni, momwe sitinali woyenera kulandira chikondi chimenechi, popeza tinali nkhandinkha ndi wodetsedwa ndi uchimo kotero pamafunikadi wina amene angatitsuke ndi mwazi wake. Uyu, ndiye Kristu amene ali chikondi. Tikunena kuti ichi, ndichikondi chomwe simungachipezem'chilengedwe cha munthu, koma kudzera m'mwazi wa Mwana Wankhosa, wophedwa chifukwa cha machimo anu ndi anga. Taonani Paulo pa Aroma 5:7, akunena kuti, "Pakuti ndi chibvuto munthu adzafera wina wolungama; pakuti kapena wina adzalimbika mtima kufera munthu wabwino."Ndiye ndifuna muone kuti ngati inu simungapeze munthu wina kukuferani inu, ndiye kuti muli pamabvuto. Koma pano Mulungu wangoonetseratu chikondi chake pakupereka mwana wake kuti afere inu komanso ine, amene

sakapezeka wina wondifera. Komanso taonani kuti chikondi chimenechi, chinaoneka pamene “Tinali chikhalire ofoka, pa nyengo yake Kristu anawafera osapembedza. Koma Mulungu akutsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Kristu anatifera ife” (Aroma 5:6, 8). Ndiye mwa mau amenewa ndikobvuta kuti ife, tifotokonze za chikondi chomwe chimapezeka mwa Mulungu popeza ife tilibe ndipo kuti ife sitinakondepo wina. Kodi inu mudachilawa kale chikondi chimenechi?

Tsono pamene Mtumwi Yohane akunena kuti, “Mulungu anamtuma Mwana wake wobadwa yekha, alowe m’dziko lapansi” akuonetsa ndime ina momwe anthu ena afuna kutichotsera umulungu wa Kristu. Taonani pamene Ambuye Yesu Kristu akutchedwa “Mwana wake Wobadwa yekha,” zikutanthauza kuti Kristu ali paubale wapadera-dera ndi Atate. Uyu, ndiye amene sanalengedwa. Mukumbukira kuti Mulungu anatchaangelo kuti ndi ana ake ndipo amanenanso kuti iwo amene akhulupirira Kristu ndi ana a Mulungu, koma akumutchula Ambuye Yesu Kristu kuti ndiye “Mwana wake Wobadwa yekha.” Ndiye ndikuchitanso chidwi kuti

dzina ililikuperekedwanso kwa Isake, kuti iye amene analandira mapangano/malonjezano anapereka nsembe mwana wake yekha. Tsono pa Ahebri 11:17, tipeza mau akuti, “Ndichikhulupiriro Abraham, poyesedwa, anapereka nsembe Isake, ndipo iye amene adalandiramalonjezano anapereka mwana wake wayekha.”Ndiye chimene chikundichititsa chidwi ndi chakuti, mau akuti Abraham “anapereka mwana wake wayekha,” pamene anali kale ndi mwana wina wotchedwa Ismayeli. Koma Isake akutchulidwa kuti ndiye mwana wake m’modzi yekha. Kodi inu mukuganiza kuti panali chifukwa chanji?Yankho likuti uyu, anali mwana wapadera-dera chifukwa kubadwa kwake kunali kodabwitsa ndipo analinso pachiyanjano chodabwitsa ndi atate wake, chomwe Abraham samagawana ndi mwana wina aliyense. Momwemonso ubale womwe ulipomuutatuwa Mulungu ndi wakuti Kristu ndiye Mwana wachikhalire wa Atate amuyaya. Kutanthauza kuti sitingakhale ndi Atate amuyaya popanda kukhala ndi Mwana wamuyaya.Koma tiyenera kudziwa kuti Mulungu si atate monga mwa thupi ayi.Kumbukirani Yohane 4:24, adanena kuti Mulungu ndiye Mzimu.” Tere, tikunenetsa kuti Ambuye Yesu Kristu ndiye Mwana wa Mulungu wodabwitsa, popeza ena onse ndiwo wolengedwa

monga Adamu ndi angelo. Komanso ena atchulidwa ana a Mulungu chifukwa chakubadwamwatsopano, koma Yesu ndiye wodabwitsa kwambiri.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti Yohane 1:14, akunena kuti, “Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa Wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi.” Tsono taonani kuti Mwana uyu, anatumizidwa m’dziko momwe muli anthu ochimwa kotero kuti anadza ndi cholinga chofuna kuwachotsera machimo awo, koma ndikumalo komwe ananyozeka ndi kuzunzikako. Kotero kuti kumapeto a zonsezi, anaphedwa, kukwaniritsa cholinga cha utumiki wake kuti ife wochimwafe, amene tinali akufa mwa Adamu, muuchimo, akuda m’chilamulo, amene sitikanathakudzipatsa moyo tokha, koma Kristu anafa ndi kuuka kuti tikakhale ndi moyo kudzera mwa Iye. Kutanthauza kuti zotsatira zaimfa ndi kuuka kwa akufa kwa Kristu, inu ndi ine, tinakhala ndi moyo muuzimu ndi cholinga chakuti tikakhale m’chiyero chake. Kodi moyo umene mulinawo, mukutsimikiza mtima kuti mukukhala m’moyo wa Kristu?

10. Umo muli chikondi, sikuti ifetinakonda Mulungu, koma kuti Iye anatikonda ife, ndipo anatuma Mwana wake akhale chiombolo chifukwa cha machimo athu.

Mundime iyi, Yohane akunena kuti Ambuye Yesu anaperekedwa m'dziko lapansi kuti akhale chiombolo cha machimo athu ndi a dziko lonse lapansi monga mwa mau apa 1 Yohane 2:2. Ndiye pamene tiona tanthauzo la chiombolo, tikupeza kuti likufanana ndi gome lotetezeram'chipindachoyeretsesa. Kutanthauza kuti monga Yesu akutchulidwa kuti ndiye chiombolo chathu, akunena kuti ndiye gome lotetezera machimo athu. Tere tikutsimikizadi kuti Yesu Kristu ndiye chotetezera chathu popeza anafa kuti ombolakuchilango cha machimo athu (Aroma 4:25). Tsono pamene tibvomereza kuti Kristu anakhala chiombolo cha machimo athu, ndipo pamene timadza molimba mtima kumpando wachisomo wa Mulungu, popeza pali chifundo chomwe chili chikhalire kuyembekezera inu ndi ine. Ndiye tikunenetsa kuti Mulungu anaonetsa chikondi chake kudzera muimfa ndi kuuka kwa akufa kwa Ambuye Yesu Kristu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti pamene tikuti Mulungu ndiye chikondi, sizitanthauza kuti akhoza kungotitsegulirakhomolakumwamba chifukwa cha chikondichi ayi. Ife tiyenera kudziwa kuti Mulungu uyu ndiye wolungama ndi woyera mtima, kotero kuti akalandira inu ndi ine, chifukwa cha chiyero chomwe tirinacho mwa Ambuye wathu Yesu Kristu. Tikunena kuti kulungama kwa Mulungu kudaonekera pamene anapereka Mwana wake yekha kuti afe kuti akhozekulipadipo la machimo anu ndi anga kenaka Mulungu akhoza kutifikira ndi kutipulumutsa. Ichi ndicho chikondi cha Mulungu momwe anatipulumutsaife, osati chifukwa chooneka bwino ayi, popeza tinali chikhalire muuchimo wathu. Tsono pachifukwa chakuti Mulungu anapereka chiombolo pamene tikanali muuchimo, Leronso, inu mukhoza kupanga chisankho chakudzakwa Iye popeza khomo la kudza kwa Iye anatsegula kudzera mwa Yesu Kristu amene akudzitchula kuti ndiye Njira ndi khomolofikira kwa Atate (Yoh.14:6). Tere tikunenetsa kuti ndizosathandizakungodalira kuti Mulungu ndi chikondi popeza Iye sapulumutsa ndi chikondi ayi, koma ndi chisomo chake.

11. Okondedwa, ngati Mulungu anatikondaife kotero, ifenso tiyenera kukondana wina ndi mnzake.

Mtumwi Yohane pano akuti, popeza Mulungu waonetsera chikondi chake pa ife, ndikoyenera kuti pachifukwa chimenechi, tikondane wina ndi mnzake. Tsono nkhani kuti popeza Mulungu Wamkulukulu, adakondaiwo ngakhale amene ali pansu peni-peni, iwo osadziwikamkomwe ndi wosayenera, ifenso tiyenera kuwakonda iwo popeza ndinjira yokhayo yomwe tingaonetsere kuti tiri ndi Mzimu wa Mulungu. Komanso tiyenera kukondana wina ndi mnzake popeza chikondi chimafunitsitsa kuti aliyense akhale pachisangalalo. Kodi inu, mulinawo mtima woterewu?

Ndiye pamene Mtumwi Yohane akunena kuti, “Ngati Mulungu anatikonda ife, koterofenso tiyenera kukondana wina ndi mnzake.” Mwanjira ina Yohane akunena kuti chikondi cha Mulungu pa ife, ndicho chiyenera kutikakamiza ife kukonda anzathu. Kunena kuti chitsanzo cha Mulungu ndichimene chiyenera kutikakamizaife kukonda ena. Ife wokhulupirira tiyenera kukhala wotsanza Mulungu monga ana ake. Kunena kuti kumene kutsanukira chikondi cha Mulungu, ifenso tiyenera kupereka chikondi chathu

komweko. Kapena tifunse kuti, kodi ndikoyenera kukana kukonda, chomwe Mulungu wamuyaya adachikonda? Inu ndi ine, ngati akristu, tiyenera kukhala wokhumba kukonda chomwe Mulungu akonda, kapena kukonda omwe Mulungu akonda. Kutsimikiza kuti chikondi chotere cha Mulungu ndicho chimene chimafulumiza anthu onse kukondana wina ndi mnzake. Ichi, ndichimene Ambuye Yesu Kristu adanena pa Mateyu 5:45, pamene adati, “Kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba; chifukwa Iye amakwezera dzuwa lake pa oipa ndi pa abwino, namabvumbitsira mvula pa olungama ndi pa osalungama.” Tsono nkhani ikuti chikondi chotere chodabwitsa cha Atate, chomwe chikuonetsedwa ku mpingo wake ndi kwa woyera mtima wonse, chiyenera kukhala chopindula kwa ena onse.

Tiyeni titsirize ndi mau akuti pamene Yohane akunena kuti, ife tiyenera kukondana wina ndi mnzake, sakunena za chikondi cha masewera ayi. Tamvani Ambuye Yesu pa Yohane 14:15, akunena kuti, “Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga.” Ndipo pa Yohane 15:12, Yesu mwini akuti, “Lamulo langa ndi ili, kuti mukondande wina ndi mnzake, monga ndakonda inu.” Ndiye

pamau awa, kodi inu mukhoza kuda akristu anzanu ndi kupitiliza kukonda Mulungu?Ndiye tikunenetsa kuti ngati inu simungaonetse chikondi pa ena ndichosamveka kuti inu mukhoza kukonda Mulungu.

Kwalerotilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 1 Yohane 4:7-11, pa mutu wakuti akristu ayenera kukondana wina ndi mnzake.

Ambuye akulitse chisomo chake mwa inu, pamene mukondaiwo amene Mulungu awakonda. Amen!